## UNDUNA WA ZACHILENGEDWE


NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

**NYENGO MSABATAYI**

**KUYAMBIRA PA 16 MPAKA PA 22 MARCH, 2026**

### NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI


Tiyembekezere nyengo **yamvula ya mabingu m'madera ambiri yomwe idzigwa ya mphamvu** maka m'madera am'phepete mwa nyanja ya Malawi **monga ku Salima ndi madera ozungulira** kuyambira pa 16 March mpaka lachitatu pa 18 March 2026 kamba ka dera la mphweya lopepuka lomwe lili m'dziko muno. Kenako, mvula idzayamba kuchepa mphamvu mpaka kumapeto a sabatayi.




*Ulosi wamvula kuphatikiza masiku onse musabatayi*

### NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

Kunali nyengo yamitambo ndi yozizira mmadera ambiri komanso mvula yomwe inagwa yamphamvu maka m'madera akumpoto ndi kumwera. Mvula yambiri m'maola 24 yomwe tinalandira kuchokera kumwera inali **166.4mm** kuchokera ku Matandani **station ku Zomba pa 14 March, m'chigawo chapakati inali 87.2mm kuchokera ku Salima pa 15 March** pomwe kumpoto inali yamlingo wa **102.3mm kuchokera ku Kazuni ku Karonga pa 12 March 2026.**




*Mapu akuonetsa mvula yochuluka yomwe talandira mu sabatayi kuyambira pa 09 mpaka 15 March 2026*

### LANGIZO M'SABATAYI:

**Madzi osefukira:** Pomwe mvula ikuyembekezereka kugwa yamphanvu maka madera amphepete mwa nyanja ya Malawi monga ku Salima ndi nkhotakota, tipewe kuoloka madzi omwe asefukira komanso akuthamanga.

**Chiopsezo cha napolo:** Pomwe mvula ikugwa kwa masiku angapo, chiopsezo cha napolo ndi chachikulu makamaka madera amchigawo cha kummwera, monga Blantyre, Mulanje, Chiradzulu ndi Thyolo.

***For further information please contact:*** *The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*

**Malo osindikizira: Blantyre** **Yatsindikizidwa Lamulungu pa 15 March, 2026.**